

Munthu Wodzichepetsa Ndiponso Wolimba Mtima

YONA—GAWO 1

Malangizo: Chitani zotsatirazi muli pamalo opanda phokoso. Pamene mukuwerenga mavesiwo, yerekezerani kuti nkhaniyo ikuchitika inuyo muli pomwepo. Yesani kuona m'maganizo mwanu zimene zikuchitika. Mukhale ngati mukumva zimene anthuwo akulankhula. Yesani kumva mmene anthu a m'nkhaniyi akumvera.

**① ONANI NKHANIYI BWINOBWINO.—WERENGANI YONA 1:1-17;
2:10-3:5.**

Kodi mukuganiza kuti panyanjapo pankhoneka bwanji ndiponso pankamveka phokoso lotani chifukwa cha mphepo yamkutho? _____

Kodi mukuganiza kuti zimene Yona ndiponso anthu oyendetsa chombocho ananena zikusonyeza kuti ankamva bwanji mumtima mwawo? _____

Fotokozani zimene Yona ayenera kuti ankaganiza panthawi imene ankamira m'nyanja ndiponso ali m'mimba mwa chinsomba. (Werengani Yona 2:1-9.) _____

② FUFUZANI MOZAMA.

Kodi ku Nineve kunkakhala anthu otani, nanga n'chifukwa chiyani poyamba Yona sana-fune kuwalalikira anthu amenewa? (Nahumu 3:1) _____

Kodi mukuganiza kuti n'chifukwa chiyani Mulungu ankaona kuti Nineve unali “mudzi waukulu pamaso” pake? (Yona 3:3; 2 Petulo 3:9) _____

Popeza kuti Yona ananena zoonza zokhazokha za tchimo lake ndiponso za Mulungu,

kodi zimenezi zikusonyeza kuti iye anali munthu wotani? (Werenganinso Yona 1:9, 10.)

Kodi Yona ayenera kuti anadziwa bwanji zimene zinachitika m'chombocho iye ataponyedwa m'nyanja? (Werenganinso Yona 1:15, 16.)

3 GWIRITSANI NTCHITO ZIMENE MWAPHUNZIRA. LEMBANI ZIMENE MWAPHUNZIRA PONENA ZA . .

Mantha.

Kudzichepetsa.

Kulimba mtima.

Mmene Yehova amaonera anthu ngakhale amene timawaona kuti ndi oipa kwambiri.

4 M'NKHANIYI, KODI NDI MFUNDO ITI IMENE YAKUKHUDZANI KWAMBIRI NDIPO N'CHIFUKWA CHIYANI?

Kuti mudziwe zambiri, werengani *Nsanja ya Olonda* ya January 1, 2009, tsamba 25 mpaka 28.

